## PHUNZIRO LA 20

1. Ngakhale kuti makolo athu amkamukana Mulungu, kodi Mulungu anazisiya zimene anakhoza zotumiza Mpulumutsi?
-Iyayi.

2. Chifukwa chakuti makolo athu anakana kumumvera Mulungu, kodi Mulungu anasankha ndani kuti atumize Mpulumutsi kupitira mwa iye?
-Abulamu.

3. Kodi Mulungu anasankha Abulamu chifukwa chakuti anali osachimwa?
-Iyayi.
-Abulamu anabadwira mu tchimo.

4. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamusankha Abulamu?
-Abulamu amkakhulupilira kuti tchimo lake limkayenera kulandira chilango cha imfa.
-Abulamu amkakhulupilira kuti Mulungu yekha ndi amene anali oyenera kumupulumutsa iye.
-Abulamu amkakhulupilira kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi.

5. Abulamu anakwatira mkazi dzina lake Sarayi.
-Kodi Abulamu ndi Salayi anali ndi ana angati?
-Palibe.

6. Kodi chifukwa chiyani Abulamu ndi Salayi analibe ana?
-Chifukwa chakuti Sarayi anali osabereka.

7. Kodi Mulungu anamuwuza Abulamu kuti achite chiyani?
-Mulungu anamuwuza Abulamu kuti achoke ku dziko lake, ndipo apite kumene Mulunguyo akamutsogolere iye.

8. Kodi Mulungu anamulonjeza chiyani Abulamu?

-Choyamba, Mulungu anamulonjeza Abulamu kuti adzakhala ndi zidzukulu zambiri zimene zidzakhale mtundu wawukuru.
-Chachiŵiri, Mulungu anamulonjeza Abulamu kuti adzamudalitsa.
-Chachitatu, Mulungu analonjeza kuti adzaŵadalitsa anthu onse amene adzamudalitse Abulamu, ndipo adzaŵatembel-era anthu onse amene adzamutembelere Abulamu.
-Chachinayi, Mulungu analonjeza kuti adzaŵadalitsa anthu onse kupitira mwa chidzukulu chimodzi cha Abulamu.

9. Kodi chidzukulu cha Abulamu chimenechi ndi ndani, chimene anthu onse adzadalitsika kupitira mwa icho?
-Mpulumutsi.

10. Kodi Mpulumutsi adzapanga chiyani?
-Mpulumutsi adzabwera kudzagonjetsa mphamvu ya tchimo.
-Mpulumutsi adzabwera kudzagonjetsa mphamvu ya imfa.
-Mpulumutsi adzabwera kudzagonjetsa mphamvu ya Satana.
-Mpulumutsi adzamugonjetsa Satana, ndikuŵanjanitsanso anthu ndi Mulungu.

11. Kodi Abulamu amkakhulupilira m'malonjezo a Mulungu?
-Inde.

12. Kodi Abulamu anachita chiyani, Mulungu atapereka malonjezo amenewa?
-Mulungu atapereka malonjezo kwa Abulamu, Abulamu anatenga mkazi wake Salayi, mwana wa mng'ono wake, Lo-ti, ndi chuma chake chonse, ndipo anamutsatira Mulungu ku-mene Iye anaŵatsogolera.

13. Kodi Mulungu anamutsogolera Abulamu kupita kuti?
-Mulungu anamutsogolera Abulamu kupita ku malo atsopano kotchedwa Kanani.

14. Mulungu analankhula kwa Adamu ndi pakamwa pake.



-Kodi chifukwa chiyani Abulahamu anaseka?
-Kodi Abulahamu anaseka chifukwa chakuti samkamu-khulupilira Mulungu?
-Iyayi.

-Abulahamu anaseka chifukwa chakuti anali ndi zaka 100, ndipo Sara anali ndi zaka 90, ndipo Mulungu amkafuna kuti aŵapatse mwana wa mamuna.

-Kodi Mulungu anakatha kumupatsa mamuna wa zaka 100, ndi mkazi osabereka wa zaka 90, mwana wamamuna ?
-Inde.

-Kodi pali chinthu china chilichonse chimene chili chovuta kwa Mulungu?
-Palibe.

-Kodi amene analenga munthu wamamuna woyamba anali ndani?
-Mulungu yekha.

-Kodi amene analenga munthu wamkazi woyamba anali nda-ni?
-Mulungu yekha.

-Kodi amene amapereka moyo kwa mwana aliyense ndi nda-ni?
-Mulungu yekha.

-Kodi pali chinthu china chilichonse chimene sangachithe ku-chichita Mulungu?
-Palibe.

-Mulungu angathe kupereka mwana wa mamuna kwa mamuna wa zaka 100 ndi mkazi wosabereka wa zaka 90.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 17:15-16

15-Mulungu anamuwuzanso Abulahamu kuti, “Mkazi wakoyu usamutchulenso kuti Sarayi. Tsopano dzina lake ndi Sara.

16-Iyeyu ndidzamudalitsa ndipo adzakubalira mwana wamamuna. Ndidzamudalitsa ndipo adzakhala mai wa mitundu ya anthu. Pakati pa zidzukulu zakezo padzatuluka mafumu.”

-Kodi dzina latsopano limene Mulungu anamupatsa Sarayi linali ndani?
-Sara.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamupatsa Sarayi dzina latsopano?
-Chifukwa chakuti Sarayi adzakhala ndi zidzukulu zambiri.

-Ngakhale kuti Sarayi anali osabereka ndiponso wokalamba, Mulungu anamulonjeza Sarayi kuti adzakhala mai wa zidzukulu zambiri.

-Ngakhale kuti Sarayi anali osabereka ndiponso wokalamba, Mulungu anamulonjeza Sarayi kuti adzabereka mwana wa mamuna.

Tiyeni tiŵerenge zimene anachita Abulahamu pamene Mulungu anamulonjeza zimenezi:

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 17:17

17-Apo Abulahamu anagwada pansi. Anayamba kuseka, nati, “Kodi mamuna woti ali ndi zaka 100, angathe kuberekanso? Kodi Sara, amene ali ndi zaka 90, angathe kuberekanso?”



Kodi nanga Mulungu amalankhula bwanji kwa anthu masiku ano?
-Kupitira M’buku lake, Bayibulo.
-Kodi mukumukumbukira Loti?
-Loti anali mwana wa mng’ono wake wa Abulamu, amene anatsagana naye popita ku Kanani.

-Tsiku lina panali vuto pakati pa Abulamu ndi Loti.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 13:5-7

5-Loti amene amkayenda limodzi ndi Abulamu, anali ndi nkhosa, mbuzi ndi ng’ombe pamodzi ndi banja lale ndi atchito ake amene amkakhala naye limodzi.

6-Tsopano malo odyetserapo ziweto anali osakwanira kwa aŵiriwo, chifukwa chakuti aliyense anali ndi zoweta zambiri.

7-Chomcho panabuka mkangano pakati pa abusa a Abulamu ndi Loti.

-Kodi vuto limene linalipo pakati pa Loti ndi Abulamu linali lotani?
-Abulamu anali ndi ng’ombe ndi nkhosa zambiri.
-Loti nayenso anali ndi nkhosa ndi ng’ombe zambiri.

-Chifukwa chakuti Abulamu ndi Loti anali ndi nkhosa ndi ng’ombe zambiri, kunalibe msipu okwanira woti mkumadyetsera ziweto zawo zonse.

-Kodi Abulamu anaganiza zochita chiyani pofuna kuthetsa vuto lawowolo?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 13:8-9

8-Tsopano Abulamu anamuwuza Loti kuti, “Ife ndi pachibale, chomcho pasakhale kukangana pakati pa ine ndi

iwe, ndiponso abusa ako sayenera kukangana ndi abusa anga.

9-Tiyeko tisiyane, usankhe dera lililonse la dziko lino limene ukufuna. Iwe ukapita mbali ina, ine ndipita ku mbali ina.”

-Abulamu anaganiza zakuti asiyane ndi Loti.
-Abulamu anaganiza zakuti Loti asankhe kumene akakhale.

-Loti akasankha ku chigwa , Abulamu akakhala ku dera la mapiri.
-Loti akasankha ku dera la mapiri, Abulamu akakhala ku chigwa.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 13:10-11

10-Chomcho Loti atayang’anayang’ana, anawona kuti chigwa chonse cha mtsinje wa Yolodani mpaka ku Zowari, chili ndi madzi ambiri.Chigwacho chinali ngati munda wa AMBUYE kapenanso ngati dziko la Iguputo.

11-Loti anadzisankhira chigwa chonse cha Yolodani, napita kukakhala chakuvuma. Umu ndi m’mene anthu aŵiriwo anasiyanirana.

-Loti anasankha kukakhala ku chigwa.

-Kodi chifukwa chiyani Loti anasankha kukakhala ku chigwa?
-Chifukwa chakuti kunali msipu wambiri wodyetsera ziweto zake.
-Loti amkangoganizira za msipu wokha.
Loti amkangoganizira za ziweto zake zokha.
-Loti amkangoganizira za chuma chake chokha.

-Loti anapanga chisamkho choyipa chokakhala ku chigwa.
-Kodi chifukwa chiyani Loti anapanga chisamkho choyipa?

-Chifukwa chakuti Loti sanamufunse Mulungu chimene

-Mulungu akuzidziŵa zimene zidzatiwonekere ife chaka cha maŵa.

-Mulungu yekha ndi amene akuzidziŵa zimene zidzatiwonekere ife mtsogolo.

-Pamene Abulamu anali ndi zaka 99, Mulungu analankhulanso kwa Abulamu.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 17:1-5

1-Abulamu ali ndi zaka 99, AMBUYE anamuwonekera namuwuza kuti, “Ine ndine Mulungu Mphambe. Udzindimvera nthaŵi zonse, ndipo udzichita zolungama.

2-Ndidzachita nawe chipangano; ndipo ndidzakupatsa zidzukulu zambiri.”

3-Nthaŵi yomweyo Abulamu anagwada pansi ndipo Mulungu anati,
“Nachi chipangano chimene ndidzachite nawe. Ndikulonjeza kuti udzakhala kholo la anthu a mitundu yambiri. Dzina lako silidzakhalanso Abulamu, koma Abulahamu. Limeneli ndilo dzina lako, chifukwa chakuti ndikukusandutsa kholo la anthu a mitundu yambiri.

-Mulungu analankhula kwa Abulamu, ndipo anamupatsa iye dzina latsopano.
-Kodi dzina latsopano limene Mulungu anamupatsa Abulamu linali ndani?
-Abulahamu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamupatsa Abulamu dzina latsopano?
-Chifukwa chakuti Abulamu adzakhala ndi zidzukulu zambiri.

-Mulungu anamupatsanso Salayi dzina latsopano.

akapolo kumeneko, ndipo zidzazunzika kwa zaka zokwana 400.
14-Koma mtundu umene udzachite zimenezo, ndidzawulanga, ndipo zidzukulu zakozo, zidzatenga chuma chambiri potuluka m'dzikomo.
15-Tsono iwe udzakhala ndi moyo mthaŵi yayitali ndipo udzafa mwamtendere. Udzayikidwa m'manda utakalamba kwambiri.
16-Pakadzapita mibadwo inayi, zidzukulu zakozo zidzabwereranso kuno, chifukwa chakuti sindidzaŵathamangitsa a Amori mpaka kuyipa kwawo kudzafike pachimake penipeni kuti adzalangidwe."

-Mulungu analankhulanso kuti zidzukulu za Abulamu zidzapita kukakhala ku dziko lina, koma pakadzatha zaka 400, Mulungu adzadzibwerezanso ku Kanani.

-Kodi Mulungu anadziwa bwanji zimene zidzachitike kwa zidzukulu za Abulamu?
-Mulungu anali atadziwa kale zonse zimene zidzachitike kwa zidzukulu za Abulamu, zidzukuluzo zisanabadwe.

-Kodi mukuzidziŵa zimene zidzachitike maŵa?
-Iyayi.

-Kodi mukuzidziŵa zimene zidzachitike mwezi wa maŵa?
-Iyayi.

-Kodi mukuzidziŵa zimene zidzachitike chaka cha maŵa?
-Iyayi.
-Koma Mulungu amazidziŵa zonse.

-Mulungu akuzidziŵa zimene zidzatiwonekere ife maŵa.
-Mulungu akuzidziŵa zimene zidzatiwonekere ife mwezi wa maŵa.



anakachita.
-Chifukwa chakuti loti anakana kumumvera Mulungu.

-Kayini anakana kumumvera Mulungu, ndipo anamupha mng'ona wake, Abele.

-Zidzukulu za Kayini nazonso zinakana kumumvera Mulungu.
-Zidzukulu za Kayini zonse zinafa ndi chigumula cha madzi.

-Mukamakana kumumvera Mulungu, nanunso mudzafa.

-Mukamakana kumumvera Mulungu, mudzapita ku Nyanja ya Moto Wosatha imene Mulungu anamupangira Satana ndi ziwanda zake.

-Kodi chuma chanu chidzakupulumutsani inu ku Nyanja ya Moto wosatha?
-Iyayi.

-Loti anakana kumumvera Mulungu ndipo anapita kukakhala ku chigwa.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 13:12-13

12-Abulamu anakakhala ku dziko la Kanani, koma Loti anakhazikika pakati pa mizinda ya m'chigwa, nakamanga hema pafupi ndi mzinda wa Sodomu.
13- Anthu a mu mzindawo anali oyipa kwambiri, ndipo amkaŵachimwira AMBUYE.

-Ku chigwacho kunali mizinda iŵiri.
-Mayina a mizinda imeneyi anali Sodomu ndi Gomora.

-Anthu a ku Sodomu ndi Gomora samkamukhulupilira Mulungu.

-Anthu a ku Sodomu ndi Gomora anali ochimwa kwambiri.

-Kodi Mulungu amkakuwona kuchimwa kwa anthu a ku Sodomu ndi Gomora?
-Inde.

-Kodi tingabise china chilichonse chimene tikuganiza kwa Mulungu?
-Iyayi.

-Kodi tingabise china chilichose chimene timalankhula kwa Mulungu?
-Iyayi.

-Kodi tingabise china chilichonse chimene timachita kwa Mulungu?
-Iyayi.

-Tiyeni tiŵerenge zimene Mulungu anamuwuza Abulamu, Loti atapita ku chigwa:

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 13:14-15 ndi 17

14-Loti atachoka, AMBUYE anamuwuza Abulamu kuti, “Uyang’ane bwino kumpoto, kumwera, kuvuma, ndi kuzambwe.
15-Ndidzakupatsa dziko lonse limene ukuliwonalo, iweyo pamodzi ndi zidzukulu zako. Ndipo lidzakhala lako mpaka muyaya.
17-Nyamuka tsopano, uyendere dziko lonselo, chifukwa ndikukupatsa.”

-Mulungu ananena kuti adzamupatsa Abulamu dziko lonse la kanani.

-Apa palinso zimene Mulungu ananena kwa Abulamu.



Tiyeni tiŵerenge Genesesi 15:5-6

5-[AMBUYE] anamutulutsira Abulamu panja, namuwuza kuti, ‘Tayang’ana ku thamboku, ndipo uŵerenge nyenyezizo ngati ungathe. Iwe udzakhala ndi zidzukulu zochuluka ngati nyenyezizo.”
6-Apo Abulamu anaŵakhulupilira AMBUYE, ndipo chifukwa cha chimenecho, Mulungu anamuwona kuti ndi wolungama.

-Mulungu ananenanso kuti Abulamu adzakhala ndi zidzukulu zochuluka ngati nyenyezi.

-Kodi kuli nyenyezi zingati?
-Kuli nyenyezi zambiri, zosaŵerengeka ndi munthu.

-Ngakhale kuti Abulamu analibe ana, Mulungu anamuwuza Abulamu kuti adzakhala ndi zidzukulu zambiri ngati nyenyezi.
-Ngakhale kuti Abulamu analibe ana, kodi iye anamukhulupilira Mulungu?
-Inde.
-Abulamu amkakhulupilira kuti tsiku lina Mulungu adzamupatsa mwana.

-Abulamu amkakhulupiliranso kuti chimodzi mwa zidzukulu zake chidzakhala Mpulumutsi amene Mulungu adzamutumize kudzaŵapulumutsa anthu.

-Apa palinso zimene Mulungu ananena kwa Abulamu.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 15:13-16.

13-AMBUYE anamuwuza iye kuti, “Udziwe kuti zidzukulu zako zidzakhala alendo a m’dziko la eni. Zidzakhala